

CHINSINSI CHA CHIPAMBANO



Phunziro 1, October 4, 2025



“Ukhale wamphamvu
ndi wolimba mtima
kwambiri. Usamale
ndithu kuti umvere
malamulo onse amene
mtumiki wanga Mose
anakupatsa. Usachoke
pa malamulo anga
ndipo kulikonse kumene
udzapite
udzapambana.”

Yoswa 1:7, ccl



Patapita zaka 40 zoyendayenda, mbadwo watsopano udauka, ndipo nthawi yogonjetsa dziko lolonjezedwa idakwana. Mose anamwalira, ndipo Mulungu adasankha Yoswa kuti atsogolere ana ake.

Yoswa ndi mbadwo watsopano anauzidwa kuti akhulupilire Mulungu kotheratu asanayambe kugonjetsa adaniwo.

Pamene mbadwo wamakono (ife) tiri mmalire a Kanani wakumwamba, Mulungu akuti: “Koma khala wamphamvu ndi olimbikira” (Yoswa 1:7).



Mawu oyamba (Yoswa 1:1-3):



Mose ndi Yoswa



Mmene bukhu la Yoswa liliri



Ntchito ya Yoswa (Yoswa 1:4-9):




Kupitiriza malonjezano



Mphamvu ndi kulimba mtima



Kupambana kwa ntchito





MAWU OYAMBA (YOSWA 1:1-3)

MOSE NDI YOSWA

"Ndipo atafa Mose mtumiki wa Yehova, Yehova anati kwa Yoswa mwana wa Nuni mnyamata wa Mose" (Yoswa 1:1)

Muchaputala choyamba cha buku la Yoswa, Mose amatchulidwa nthawi khumi ndi limodzi, ndipo dzina lake likupezeka mobwerezedwa mu bukhu lonselo

Pali zofanana zambiri pakati pa atsogoleri awiriwa:



Ngakhale chaputala choyamba cha bukhu la Yoswa chikulongosola kusinthana kwa utsogoleri pakati pa Mose ndi Yoswa, nkhani yaikulu ndi yokamba za Mulungu. Akulankhula kumayambiriro ndipo akutsogolera nkhani yonse. Kuonetsa kuti Mulungu ndiye mtsogoleri wa ana a Israel.



**Mulungu aonekera kwa iwo
(Eksodo 3:2-4; Yoswa 5:13-14)**



**Anapemphedwa kuchotsa
nsapato zawo (Eksodo. 3:5;
Yoswa 5:15)**



**Mulungu anawalonjeza
kuti akhala nawo (Eksodo
3:12; Yoswa 1:5)**



**Anakondwerera Pasika
(Eksodo 12:21-23; Yoswa
5:10)**



**Anaoloka m'madzi
panthaka youma (Eksodo
14:21-22; Yoswa 3:14-17)**



**Munyengo ya wina kunali
manna, ndipo ya wina
manna anasiya (Eksodo
16:4-5, 31; Yoswa 5:11-12)**



**Anatumiza azondi kuti
akazonde dzikolo
(Numeri 13:1-3; Yoswa 2:1)**



Tsopano Yoswa anali mtsogoleri wovomerezedwa wa Israeli. Amadziwika makamaka ngati msilikali, ndipo mphatso zake ndi makhalidwe ake anali ofunika kwambiri pa nthawi imeneyi mu mbiri ya anthu ake. Anali wolimba mtima, wotsimikiza pa chigamulo, wosakaikaika, wachangu, wona mtima, ankaganizira ena kuposa iyeyo, ndipo koposa zonse, analimbikitsidwa ndi chikhulupiliro chamoyo mwa Mulungu – limeneli linali khalidwe la munthu amene Mulungu anasankha kuti atsogolere gulu la nkondo la Israeli polowa mudziko lolonjezedwa.

Pamene Aisrayeli anali muchipululu, iye anagwira ntchito ngati mtsogoleri wachiwiri kwa Mose. Ndipo mwa khalidwe lake losalankhula zambiri, kukhazikika kwake pamene ena anali osadalirika, ndi kulimba mtima kwake kutsatira choonadi muthawi ya zovuta, anapereka umboni wa kuyenerera kwake kulowa m'malo mwa Mose. ngakhale Mulungu asanamupatse udindowo

MMENE BUKHU LA YOSWA LILIRI

"Mose mtumiki wanga wamwalira. Ndipo iwe ndi anthu onsewa, tsopano konzekani kuoloka mtsinje wa Yorodani kupita ku dziko limene ndiwapatse a Israyeli onse." (Yoswa 1:2)

Bukhu la Yoswa limasonyeza kukwaniritsidwa kwa malonjezano a Mulungu kwa a Israyeli pamene anawatulutsa mu Igupto kumene kuli kuwapatsa dziko la Kanani. Chiyambi (chaputala 1) ndi bukulo lonse lo linagawidwa m'magawo anayi akuluakulu:

KUOLOKA kupita ku Kanani

Yoswa 1:1-9

Yoswa 1:1-5:12

KUTENGA Kanani

Yoswa 1:10-11

Yoswa 5:13-12:24

KUGAWA dziko





Yoswa 1:12-15

Yoswa 13:1-21:45

KUTUMIKIRA kudzera mu kumvera LAMULO

Yoswa 1:16-18

Yoswa 22:1-24:33





NTCHITO YA YOSWA

(Yoswa 1:4-9)



KULANDIRA MALONJEZO

"Paliponse pamene phazi lanu liponde, ndikupatsani monga momwe ndinalonjezera Mose" (Yoswa 1:3)

Pa Yoswa 1:3, Mulungu analakhula mwa ulosi ngati kuti Kanani waperekedwa kale kwa Israyeli. Izi zikutanthauza kuti Mulungu anawapatsa chitsimikizo chokwanira cha kupambana kwa kulanda dzikolo.

Kenako anawakumbutsa malire achigonjetso chawo (Yoswa 1:4): kachigawo pakati pa mtsinje wa Yorodano (kummawa) ndi nyanja ya Mediterranean (kumadzulo), kuchokera kuchipululu (kummwera) mpake kumtsinje wa Yufurate (kumpoto).



Anatembenukira kwa Yoswa ndi kumutsimikizira kuti ngati ali wamphamvu komanso olimba mtima, palibe amene adzalimbane naye. (Yoswa 1:5-6)

Chipambano sichinali mu mphamvu za Yoswa koma kupezeka kwa Mulungu. Anamutsimikizira, monga mmene akuchitira nafe lero nati: "Ndidzakhala ndi iwe"





MPHAMVU NDI KULIMBA MTIMA

*"Paja ndinakulamula kuti ukhale wamphamvu ndi wolimba mtima.
Choncho usamachite mantha kapena kutaya mtima popeza Ine
Yehova Mulungu wako ndidzakhala nawe kulikonse kumene udzapite."
(Yoswa 1:9)*



Asanapemphe Yoswa kuti akhale ndi mphamvu ndi kulimba mtima pa nkhondo (Yoswa 1:9), Mulungu poyamba anamupempha kuti akhale ndi mphamvu ndi kulimba mtima pakumvera Lamulo (Yoswa. 1:7).

Izi ziri chonchonso masiku ano. Mulungu amatifunsa kuti tiyesetse kusunga malamulo Ake (Chivumbulutso 14:12). Izi zimafuna kulimba mtima kwakukulu ku mbali yathu.


Kumbali Yake, akulonjeza kuti "adzakhala nanu kulikonse kumene mudzapita." (Yoswa 1:9) ndikutikuthandiza kulimbana ndi nkhondo imene tikulimbana nayo. Osati nkhondo yakuthupi, koma "kulimbana ndi maufumu, maulamuliro, mphamvu za dziko la mdima, ndi mphamvu zoyipa kwambiri zauzimu zamlengalenga" (Aefeso 6:12). Kuti tichite zimenezi, watipatsa zida zofunika (Aefeso 6:13-17).

Kudalira mwa Mulungu ndiye chinsinsi cha chipambano. Kuti tichite zimenezi, tiyenera kulumikizana naye tsiku ndi tsiku (Aefeso 6:18)



CHIPAMBANO CHA NTCHITO

"Udziwerenga bukhu la Malamuloli, uzilingalira zolembedwa m'menemo usana ndi usiku, kuti uchite zonse zimene zinalembedwamo. Ukamatero udzapeza bwino ndikupambana."
(Yoswa 1:8)




Kupambana kuchokera ku malingaliro aumungu sikugwirizana ndi kupambana kuchokera ku malingaliro aumunthu.

Chipambano cha dziko lapansi chimakwaniritsidwa pakuswa malamulo a Mulungu ndi a anthu, koma chipambano choona ndi chamuyaya sizingatheke choncho (Yoswa 1:8)

Tidzakwanitsa kupambana tikatsatira mfundo ndi makhalidwe omwe ali mu Lamulo la Mulungu. Koma kodi izi sizikutanthauza chipulumutso kudzera mu ntchito?

Ayi konse. Chikhulupiriro ndi Chilamulo sizikutsutsana, koma zimayendera limodzi mothandizana (Aroma 3:31). Tikamakamba za chilamulo, timakamba za mmene tiyenera kukhalira, osati mmene tingapulumutsidwire. Ubale wathu ndi Mulungu umaonekera mukumvera chifuniro chake.



“Mkristu nthawi zonse amakhala ndi mthandizi wamphamvu mwa Ambuye. Mwina sitingamvetse mmene Iye amathandizira, koma ichi tichidziwa: Iye sadzalephera konse kwa iwo amene amamukhulupirira. Ngati okhulupirira akanadziwa kuti nthawi zambiri Mulungu amawateteza ku zomwe zikanatha kuwaononga, sakanadandaula kapena kutaya chiyembekezo. Chikhulupiriro chawo chikanakhalabe cholimba, ndipo palibe vuto limene likanawagwedeza. Iwo akanadalira Mulungu kuti awapatse nzeru ndi mphamvu, ndipo Iye akanachita zazikulu kupyolera mwa iwo..”

EGW (Prophets and Kings, p. 576)